

# M'THERADI



Zikomo inu, m'bale. Zikomo inu, M'bale Hoekstra.

Madzulo abwino, ku Houston. Ine ndithudi ndikuwutenga uwu ngati mwayi wawukulu, wodzakhala kuno kachiwiri usikuuno mu Houston. Papita zaka zambiri kuchokera pamene ine ndinakhala ndi mwayi wodzakhala kuno. Ndipo ndinakhala, ndikumvetsera usikuuno kwa aliyense wa oyankhula awa.

<sup>2</sup> Ndipo tsiku lina, pamene ine ndinali nditakonzekera kwa chinthu chinachakenso, malo ena, ndipo ine ndinadziwa kuti ana amenewo anali akuyang'anizana ndi imfa, Ine ndinaganiza, "Ngati chinachake chingawachitikire ana amenewo, ine sindidzakhoha kudzikhululukira ndekha," za kusabwera kuno kudzapereka lingaliro langa ndi kudzachita zonse zomwe ine ndikanatha, kuti ndidzawathandizire amayi ndi abambo awa, ndi za ana awa, ndi kudzachita zonse zomwe ndikanatha za kupulumutsa miyoyo yawo.

<sup>3</sup> Ndipo Houston ali...ndi malo achikumbutso kwa ine. Iye ali ndi zikumbutso zambiri zazikulu zomwe ndakhala ndikuzikonda kuyambira pamene ndinabwera kuno koyamba zaka zambiri zapitazo, cha kuno ku Herald Of Faith, M'bale Kidson, ndipo kenako kumusi kuno ku nyumba yoyankhuliramo pamene ine ndinali kuno ndi M'bale Raymond Richey ndi atumiki a mzindawu.

<sup>4</sup> Ndipo kenako, ndithudi, Bambo Ayers, Bambo Kipperman, usiku umene kamera inatsimikizira kuti ine sindinkanena chirichonse chimene chinali cholakwika. Izo zinali Zoona. Ndipo pamene diso la makina a kamera linajambula masomphenya a...kapena, osati masomphenya; zenizeni. Khristu amene ife timamulalikira ndi kumukonda kwambiri, anali nafe, kuti Iye analonjeza kuti akanadzakhala nafe, ndipo kamera inajambula chithunzi Chake. Nthawi zambiri ine ndakhala ndikunena, mu nthawi zakale, kuti—kuti ine ndimakuwona Kuwala kuja nthawi zonse. Koma nthawizina anthu akhoza kumakayikira pang'ono za Iko, chimene iwe ukhoza kukhulupirira kuti iwo akhoza kukhala mwanjira imeneyo, koma usiku umenewo izo zinatsimikizira izo. Iyo inali nthawi yoyamba imene Iko kunayamba kwajambulidwapo.

<sup>5</sup> Kuyambira pamenepo, Iko kwakhala kukujambulidwa kangapo. Mu Germany posachedwapa, ndikubwera kumeneko, pamene kudzoza kunalipo, ndi pamene Iko kunabwereranso. Ndipo zinthu zimenezo sizoti zimukweze munthu winawake, koma izo ndi zoti zitsimikizire Kukhalapo kwa Yesu Khristu pakati pa anthu Ake.

<sup>6</sup> Ndipo ife tikukhulupirira kuti Ambuye Yesu yemweyo ali pano usikuuno, kuti adzatithandize ife mu nkhani iyi. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti Iye ndi wokondweretsedwa kwambiri ndi izo kuposa momwe ife tingakhalire. Ndipo ine ndithudi ndikuwamvera chisoni makolo a ana awa, ndipo phewa-kuphewa ndi mwamuna ndi mkazi aliyense amene akuyesetsa kuti awapulumentse iwo ku nsagwada za imfa.

<sup>7</sup> Ndipo, tsopano, ine ndamva kuti uwu si msonkhano wa chitsitsimutso, koma ndi chabe a—mndandanda wa misonkhano ya mapemphero imene yakonzedwera miyoyo iyi imene ili mmithunzi ya imfa. Ndipo kotero ine ndachedwa. Sindiyankhula motalika kwambiri.

<sup>8</sup> Koma ndikufuna kutenga mutu, kapena phunziro, kani, kuchokera mu nkhani imene ine ndikufuna kuti ndiwerenge mmalo awiri mu Lemba. Ndipo inu amene muli ndi Mabaibulo, ngati mungatsegule ndi ine kwa mphindi chabe, ku Bukhu la Afilipi, mutu wa 1, ndi ndime ya 20 ya mutu wa 1 wa Afilipi.

*Malingana ndi ziyembekezo zanga zowonamtima ndi chiyembekezo changa, kuti sindidzachita manyazi mu kalikonse, koma...ndi kulimba mtima konse, monga nthawizonse, koteronso tsopano Khristu adzakulitsidwa mu thupi langa, kaya izo zikhala... moyo, kapena...imfa.*

<sup>9</sup> Ndipo kenako mu, aponso, mu Bukhu la Machitidwe, mutu wa 2 ndi ndime ya 30. Ndikhoza kuweringa ya 25 mpaka 30.

*Pakuti Davide anayankhula zokhudza iye, pakuti ine ndinawawoneratu Ambuye nthawizonse pamaso panga, pakuti iye ali kudzanja langa lamanja, kuti ine ndisasunthidwe:*

*Chifukwa chake mtima wanga unakondwera, ndipo lirime langa linakondwera; komanso thupi langa lidzapuma mu chiyembekezo:*

*Chifukwa Ine sindidzasiya moyo wanga ku gehena, ngakhalenso Ine sindidzalola Woyera Mmodzi wanu kuti awone chivundi.*

*Inu mwandidziwitsa ine njira ya moyo; inu mudzandidzaza ine ndi chimwemwe ndi mawonekedwe anu.*

*Amuna ndi abale, lolani ine ndiyankhule momasuka kwa inu za mbadwa yakale Davide, kuti iye ali zonse ziwiri wakufa ndipo anayikidwa mmanda, ndipo manda ake ali ndi ife kufikira tsiku lino.*

*Chotero pokhala mneneri, ndi podziwa kuti Mulungu analumbirira ndi lumbiro kwa iye, kuti mwa chipatso cha m'chuuu mwake, malingana ndi thupi, iye*

*adzamuwukitsa Khristu kuti adzakhale pa mpando wake wachifumu;*

*Iye powoneruta izi kale ankayankhula za kuwuka kwa Khristu, kuti moyo wake sunasiyidwe mu gehena, ngakhale thupi lake silinawone chivundi.*

<sup>10</sup> Tiyeni tiweramitse mitu yathu mphindi chabe kwa pemphero.

<sup>11</sup> Atate athu Akumwamba, ife ndi oyamikira kwa Inu chifukwa cha chifundo. Ndipo izo ndi moona, Ambuye, chifukwa chimene ife tiri pano usikuuno, ndi kuti tidzapemphe chifundo. Ife sitikanafunsa izi ngati ife tikanakhala kuti tinalibe chikhulupiriro choti tikhulupirire kuti izo ziperekedwa kwa ife. Amuna awuluka kuzungulira dzikoli, ndipo mapemphero akupita kulikonse, kwa Inu, kuti miyoyo ya awa amene ife tikwapembedzera mowonamtima usikuuno ipulumutsidwe. Ambuye, ife tikupempha mphamvu kwa azimayi ndi azibambo a anyamata awa.

<sup>12</sup> Ndipo monga ife tikumvera, kuti, mnyamata wamg'ono uyu watembenezira moyo wake kwa Inu ndipo akufuna kuti azikutumikirani Inu. Ndipo monga ife tinamvera mmodzi wa oyankhula akunena, kuti, iye ankafuna kuti adzakhale mtumiki wa Uthenga, ine ndikupemphera, Mulungu, kuti Inu mupereke mwayi uwu kwa mnyamata wamg'onoyu.

<sup>13</sup> Tikhululukireni ife machimo athu, yeretsani mitima yathu ku malingaliro oyipa, ndi chirichonse chimene chingakhale mu njira yathu chimene chingatchinge pemphero lathu kuti lisayankhidwe kwa anthu awa.

<sup>14</sup> Monga ife tawerengera Mawu Anu, ife tikudziwa kuti zonse kumwamba ndi dziko lapansi zidzachoka koma Mawu Anu sadzalephera. Ife tikupemphera kuti Inu muwonjezere kwa ife, mwa Mzimu Woyera, phunziro limene lingatenge, limene lingakhale chifuniro Chanu Chaumulungu mu nkhani iyi tsopano, monga tamumvera woyimirira milandu ndi ambiri akuyankhula. Ndipo ife tikupemphera kuti tipeze chimene tingachite motsatira, sitepe yathu yotsatira yoti tichite ndi chiyani. Ambuye, ife tiri pano kuti tichite izo. Tidziwitseni ife iyo, Ambuye, kudzera mu Mawu Anu. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Mwana Wanu, Ambuye Yesu. Amen.

<sup>15</sup> Nditawerenga ndime zochepezi, ndiye ndikuzindikira kuti chochitikachi ndi chachikulu, chifukwa ndi chokhudza. Ine ndimakhoza kuganiza, pamene ndinamva ndi kulandira telegalamu ya amayi ija, "Bwanji ngati ameneyo akanakhala mwana wanga wamwamuna atakhala mu mzere umenewo, kapena mwana wanga wamkazi?" Ndipo ine... Ife tikufuna kuti tiyike chirichonse chimene tingathe kwa izo.

<sup>16</sup> Ndiyeno ena akhoza kunena, "Chabwino, ilo linali gawo laling'ono chabe la Mawu, limene inu munawerenga, M'bale

Branham.” Chabwino, izo zikhoza kukhala zoon, aponso. Koma, inu mwaona, izo si—kukula, kapena kuchuluka kwa mawu. Ndi zomwe akutanthauza. Izo ndi—izo ndi basi... Chimene icho chiri, ndi lonjezo la Mulungu.

<sup>17</sup> Ndipo ine ndikufuna kuti nditenge kuchokera ku usikuuno, kuchokera ku mutu uwu usikuuno, kapena phunziro kuchokera ku awa: *Mtheradi*.

<sup>18</sup> Ndasankha mutu uwu, kanthawi kapitako, nditakhala mchipinda changa chaku motelo, chifukwa ndikuganiza kuti tsopano ife tikusowekera chinachake chenicheni, mtheradi winawake umene ife tingawugwiritsitse ndi kudziwa kuti ndi zoon. Mu ora lofunika ngati ili, ife tikuyenera kukhala ndi chinachake chimene ife tingakhale otsimikizika, kuti ncholondola, chinachake chimene tingagwireko, kuti tidziwe, momwe vutolo liliri.

<sup>19</sup> Tsopano, molingana ndi—ndi Webster, *mtheradi*, mwa iye yekha, ndi “chopanda malire mu mphamvu,” ndipo poyambirira ndi “mapeto.” Ndipo *mapeto* ndi “ameni.” Ndi mtheradi. Monga chimene icho... Amenewo ndi mathero. Ndicho chirichonse.

<sup>20</sup> Tsopano, chopindula chachikulu chirichonse chimene chinayamba chakhalapo mdziko, chakhala chitamangirizidwa ku mtundu wina wa mtheradi. Inu simungachite chirichonse pokhapokha patakhala chinachake chimene mungagwire kwa icho.

<sup>21</sup> Pamene mnyamata akufuna kukwatira mtsikana, iye akuyenera kudziwa khalidwe la mtsikana ameneyu. Kapena mtsikanayo akuyenera kudziwa khalidwe la mnyamatayo, chinachake chimene iye angakhoze kugwirako. “Kodi mwamuna uyu adzakhala mwamuna wolungama? Kodi iye adzakhala mwamuna woyenera kwa ine?” “Kodi mkazi uyu adzandipatsa ine, m’moyo, chimene ine—chimene ine ndikuyembekezera kuchokera kwa iye, kukhulupirika ndi zina zotero?” Ndipo kenako izo zikuyenera kukhala penapake pamene iwo angakhazikitse awo—malumbiro awo, akudziwa kuti pali chinachake chimene chiti chidzagwire. Ndipo ndi chifukwa chake ife timawabweretsa iwo ku tchalitchi, ndi ku Mawu a Mulungu, kuti tidzangirize mtheradi ameneyu.

<sup>22</sup> Tsopano, Paulo apa, monga ife tikuwonera, iye anali ndi mtheradi amene iye anamugwira, moyo wake wonse, kutachitika kutembenuka kwake, amene anali: moyo wokhazikika pa Khristu! Ndipo ndi malo otani kukhalapo ndi mtheradi: moyo wokhazikika pa Khristu! Unali moyo wosiyana ndi umene iye anawukhalapo nthawi ina, chifukwa iye anati, “Moyo umene ndikuwukhala tsopano,” umene unali wosiyana ndi umene iye ankawukhala.

<sup>23</sup> Ndipo inafika nthawi imene Paulo anali ndi chomuchitikira ichi chimene chinamufikitsa iye ku lingaliro ili. Pakuti, Paulo

anali munthu wopambana, wamphamvu pakati pa Ayuda, ndipo a—wazaumulungu wopambana, koma iye sanali wotsimikiza kwambiri za mayimidwe ake. Koma tsiku lina, panjira yaku Damasiko, Kuwala, Lawi la Moto, linatsika kuchokera Kumwamba. Ndipo Paulo, pokhala Myuda, ankadziwa kuti Kuwala uku, Lawi la Moto, linali Chinthu chimene chinali, Mulungu amene anatogolera anthu ake kutuluka mu Igupto. Iwo anali atatsatira Lawi la Moto ili. Chotero, pokhala Myuda, iye ananena kwa Iye, mwamsanga, “Ambuye, Inu ndi Ndani?” Iye ankamudziwa Iye ngati “Ambuye,” koma, “Inu ndi Ndani?”

<sup>24</sup> Ndipo Liwu linabwerera kuchokera ku Lawi la Moto, “Ine ndi Yesu, ndipo ndi zovuta kwa iwe kuti uzimenyana ndi zisonga.” Kuyambira nthawi imeneyo, Paulo anadziwa kuti Yehova wa Chipangano Chakale anali Yesu wa Chatsopano. Ndipo iye anali ndi chinachake chimene iye akanakhoza kugwirako, ndipo umo ndi momwe iye anakhozera kulemba Bukhu lopambana lija la Ahebri.

<sup>25</sup> Tsopano, ngati iwe, ngati mmoyo wako uli nawo mtheradi, iwe umachita zinthu zimene mwachizolowezi sukanati uzichite, makamaka ngati uli ndi moyo wokhazikika pa Mulungu. Moyo wokhazikika pa Mulungu umapangitsa munthu kuchita zinthu zimene mwachizolowezi sakanazichita; zosamvetsetseka kwambiri, zachilendo. Nchifukwa chiyani moyo wa Chikhristu umakhala wosamvetsetseka kwambiri komanso wachirendo? Ndi chifukwa chakuti iwo amayang’ana ku Mawu a Mulungu, amene ali pafupifupi achilendo kwa dziko lero.

<sup>26</sup> Tsopano, ife tiri nawo matchalitchi, ndipo ife tiri nawo mabungwe, ndipo ife tiri ndi chipembedzo, oh, zochuluka za izo, kuzungulira dziko.

<sup>27</sup> Mu kuzungulira kwanga kasanu ndi kawiri, kuyambira pamene ine ndinali ndi inu kuno ku Houston, ine ndapeza chidziwitso chochuluka pa milungu ndi zipembedzo za dziko lino. Koma izo si zomwe ine ndikuzikamba.

<sup>28</sup> Ine ndikukamba za mtheradi, wolumikizidwa ndi Khristu. Ndiye, zimakupangani iwe kukhala—munthu wosamvetsetseka. Iwe umachita zinthu zosamvetsetseka. Kaganizidwe kako conse kamakhala kosiyana kwambiri ndi momwe unkaganizira kale, chifukwa iwe wapeza chinachake, kuti wazika chikhulupiriro mwa Winawake amene analenga kumwamba ndi dziko lapansi, kuti, Mawu Ake omwe Iwoeni ndi olenga, Mulungu Amene anayankhula ndipo dziko linakhalapo, ndipo palibe chinthu chomuvuta Iye. Kotero izo zimakupanga iwe kukhala wolenga, iwemwini, chifukwa iwe ukumatenga Mawu Ake. Ndipo mawu ndi ganizo lofotokozedwa.

<sup>29</sup> Tsopano, Paulo anali atafika mu chikhalidwe chimenecho, pamene iye anali—analibe chomuchitikira cha maphunziro azaumulungu, zonse pamodzi, koma iye anali ndi umboni

waumwini. Iye anali atakumana ndi Mulungu, ndipo anadziwa kuti iye anayitanidwa ndi Mulungu. Ndipo—ndipo palibe amene ankayenera kumuwuza iye kalikonse za zimenezo. Iye anali wotsimikiza mwamtheradi kuti Mulungu anali akanali Mulungu. Ngati dziko likanati lichite zimenezo!

<sup>30</sup> Ndipo ngati gulu ili usikuuno, lakhala pano, likanangokumbukira kuti Mulungu akanali Mulungu! Iye ndi wokhoza basi kuyankha mu nkhani iyi monga Iye aliri mu nkhani ya machiritso Auzimu kapena china chirichonse. Iye akanali Mulungu. Ndipo ngati ife tingamange ziyembekezo zathu, osati ziyembekezo zathu zokha, koma lathu—lingaliro lathu lovomereza, pa chimene Iye anena! Ndipo ife nkudziwa kuti Icho ndi Choonadi.

<sup>31</sup> Ndipo anthu amachita mwachirendo. Iwo amawoneka kuti amangoyiwala za mbali yolakwika chifukwa iwo apeza mtheradi, chifukwa iwo ndi Mawu a Mulungu. Yesu anati, “Kumwamba ndi dziko lapansi zidzachoka, koma Mawu anazi sadzalephera konse.” Koteru ngati ife tiri ndi Mawu a lonjezo, ndiye palibe kulephera kwa Iwo. Iwo sangakhoze kulephera.

<sup>32</sup> Koteru ine—ine ndikukhulupirira kuti icho ndi chifukwa chimene misonkhano ya mapempheroyi kuno, a—anthu achipembedzo aku Houston, ali ndi chidwi nayo, miyoyo ya anthu. Ndipo icho ndi chimene ife tasonkhanirana pano, ndi kuti—ndi kuti tidzaitanire pa mphamvu imene ili yoposa malamulo ndi mphamvu zonse zopangidwa ndi munthu, chinachake, Amene angathe kusintha mitima ya anthu, monga Iye anachitira kwa Farao mu Igupto. Ndipo Iye—Iye ndi Mulungu. Ndipo ife tikuyenera kusiya tsopano kumayang’ana ku—mbali yolakwika, ndi kuyamba kumayang’ana ku mbali yabwinoyo.

<sup>33</sup> Ndipo inu musanakhale ndi chikhulupiriro, inu mukuyenera kukhala ndi chinachake choti muyikepo chikhulupiriro chanucho. Ndipo ndi chiyani chinanso chimene inu mungachidalire kuti muyikepo chikhulupiriro kuposa Mawu a Mulungu wamoyo, amene analenga, mphamvu za Wamphamvuzonse? Ndi chiyani chinanso chimene tingayikepo ziyembekezo zathu? Koteru zimakupangitsa iwe kumawoneka mosinthika, kumachita mosinthika. Iwe umayang’ana kwa Mulungu kuti akwaniritse lonjezo Lake. Ndipo pamene zovuta ziwuka, monga ife tiri nazo tsopano, Iwo amakhala nangula. Iwo ndi chinachake chimene—chimene chimakugwira iwe, chinachake chimene iwe wamangiriridwako. Ilo ndi lonjezo limene ife tamangiridwako, Mawu a Mulungu ali.

<sup>34</sup> Monga momwe nangula amakhala mtheradi kwa ngalawa, mu nthawi ya namondwe. Ngalawa ikhoza kumayenda panyanja. Nangula amakhala kunja kutsogolo. Iye ndi...Iyo

imakhazikika. Anthu inu kuno ku Houston, amene muli pafupi kwambiri ndi nyanja, mumaziwona ngalawazo zikubwera.

<sup>35</sup> Ndipo nchifukwa chiyani zimanyamula kulemera kochuluka uku kwa nangula wamphamvu uyu? Koma, inu mukuwona, pamene mikuntho ibwera, a—namondwe akukukuma amene amagwedeza nyanja, ndipo amakhoza kuponyera ngalawayo ku gombe penapake, ndi kuyiphwanya iyo, kapena kuyitembuzira iyo ku madzi osaya; iyo imafika mu madzi akuya, ndi kutsitsa nangula wamkulu, wamkulu uyu, amene amakhala atamangirizika kwambiri chomwecho mpaka kuti iye amakokera pansi pa nyanja mpaka iye amakazika pamwamba pa phiri lina losawoneka. Ndiye mulole mikuntho imeneyo ikukume ngati ikufuna; iyo ili ndi mtheradi. Nangula amagwira penapake kumeneko, koma iye ndi—iye wagwiritsitsa. Ndipo pamene mafunde akuwomba mozungulira ngalawayo, iyo imakhala ndi mtheradi, chifukwa iyo imakhala kuti yamangiridwa.

<sup>36</sup> Ndipo umo ndi momwe munthu amakhalira pamene iye wamangirizidwa kwa Khristu ndi ku Mawu Ake, ndi kumawakhulupirira Iwo. Ulipo mtheradi pamenepo, chinachake chimene chikumgwira iye.

<sup>37</sup> Mtheradi umakhala ngati nyenyezi ya kumpoto pamene iwe wasochera. Pamene iwe—pamene iwe wasochera, ndipo ukufuna kupeza njira yako yobwererera, nyenyezi ya kumpoto imakhala mtheradi. Tsopano, ziripo nyenyezi zina, koma izo zimatembenuka limodzi ndi dziko. Pamene dziko likuzungulira pa izo, a...ilo limatembenuka kuchoka kwa izo. Ndipo (Kodi inu mumadziwa?), nyenyezi yaku mmawa yomweyo ndi nyenyezi ya kumadzulo nayonso, chifukwa dziko limakhala kuti langotembuzika. Koma pali nyenyezi imodzi imene simasuntha, ndipo imakhala molunjika pakati pomwe pa dziko lapansi. Ndipo kotero... Iyo ndi a—ndi nyenyezi yotsimikizika. Ngati iwe ukuidziwa nyenyezi ya kumpoto, iwe ukhoza kupeza njira yako nthawizonse. Koma, oh, apo ndi pamene munthu wasochera, ndipo iye sakudziwa basi njira yoti apiteko.

<sup>38</sup> Tsopano, ine ndikuidziwa Nyenyezi. Oh, Iyo ndi yoposa nyenyezi ya kumpoto. Ndipo kumangirizidwako ndi kuwona Kukhalapo Kwake, ziribe kanthu momwe iwe wasocherera kapena kumene iwe uli, iwe ukhoza kupeza njira yako yobwerera mwa chitsogozo Chake, amenewo ndi Mawu Ake. Iyo ndi njira yotulukira ku mavuto onse. Ndi njira ya ku mtendere. Ndi njira ya kukupambana. Ndi njira ya ku Moyo, iyoyokha, ndi kutsatira Nyenyezi iyi, Ambuye Yesu. Ndipo tsopano, ngati iwe wamangirizidwa ku Nyenyezi imeneyo, Mzimu Woyera umakhala Kampasi imene imangolozera ku Nyenyeziyo. Woyera...

<sup>39</sup> Kampasi, imakokedwa ndi maginito ku polo la kumpoto limenelo. Ndipo njira yokhayo, ziribe kanthu kuti uli mu

nkhalango yaikulu bwanji, kapena ndi thengo lochuluka bwanji lomwe lakuzungulira iwe, kapena momwe pa nyanja pali chifunga, dzanja la kampasi limenelo, iwe ukhoza kulitembenusa mwanjira iliyonse yomwe ukufuna, ndipo ilo limazungulira mmbuyo momwe ndi kuloza ku nyenyezi ya kumpoto.

<sup>40</sup> Ndipo pamene ife tiri mu vuto, ndipo tikumudalira Khristu, pali chinthu chimodzi chotsimikizika: Mzimu Woyera udzatilozera ife ku Mawu amene adzatitsogolera ife ku Nyenyezi ya Kumpoto, ndi kudzapereka zonse zimene ife tikuzisowa. Iye ndi Mtheradi wathu.

<sup>41</sup> Kwa munthu amene wasochera mnkhalango, kampasi ndi chinthu chimene chimamulondolera iye kupita kunja. Pamene ife tiri mu vuto, pali chinthu chimodzi chokha; ndi chotsimikizika basi monga nyenyezi ya kumpoto. Malingana ngati dziko layima pamalo ake, ndi kumatembenuka mozungulira, nyenyezi ya kumpoto idzakhalabe m'malo mwake.

<sup>42</sup> Ndipo bola ngati pali Umuyaya, Khristu adzakhalabe Mpulumutsi nthawizonse, ndi njira yotulukira ku vuto lirilonse, kutsemphana kulikonse, yesero lirilonse, chirichonse. Ndipo chotero ife—ife, pamene ife tiri omangirizidwa kwa Iye, ife sitimakhala okhumudwa ndi kutengeka monga momwe dziko limachitira, “Ndipo, oh, ife tichita chiyani za *ichi*? Ife tichita chiyani za *icho*?” Ife timawoneka ngati sitinazikike nkomwe. Koma munthu amene wazika moyo wake mwa Khristu Yesu, chidaliro chake pamenepo, akudziwa kuti pamene awapempha Atate chirichonse mu Dzina Lake, “Yesu anati, ‘Ine ndidzachichita icho.’” Izo zimakhazikitsa zimenezo.

<sup>43</sup> Izo—izo zikukhazikitsa izo. Izo ndi ameni. Izo ndi mtheradi. Icho ndi mapeto. Pamene Yesu anati, “Apempheni Atate chirichonse mu Dzina Langa, Ine ndidzachipereka icho,” tsopano, icho ndi mapeto. Ndi zimenezotu. “Chirichonse chimene inu mukuchisowa, pamene mupemphera, khulupirani kuti mwalandira icho, mudzakhala nacho.” Izo zikukhazikitsa izo. Ndizo zonse za izo, mwaona, ngati ife tazikika kwenikweni ndi kukhulupirira Izo, ndipo ife tamupanga Iye kukhala Mtheradi wathu. Chifukwa, Iye amatero. Iye ndi Mtheradi amene amatichotsa ife ku mantha onse. Sipamakhala mantha pamene mwamangirizidwa kwenikweni ku Thanthwe la Mibadwo.

<sup>44</sup> Sipamakhala mantha kwa wokwera ngalawa, kaya ndi mwamphamvu bwanji momwe ngalawayo ikugwedezekera ndi mafunde, bola ngati nangula ameneyo wagwira pamwamba pa phiri kumeneko. Bwanji, ndithudi. Iye amadziwa kuti ngalawayo ikhala chiliri. Iyo sipita molunjika ku thanthwe kwinakwake. Iyo siyilowa m'madzi ena osaya ndi kukatembenezika, chifukwa iyo ili ndi mtheradi wozikika pamwamba pa phiri lina.

45 Ndipo pamene munthu angathe kupemphera pemphero la chikhulupiriro, ndi kuzika moyo wake uko mu Mawu a Mulungu, mmene, “miyamba yonse ndi dziko lapansi zidzachoka, koma Mawu amenewo sangakhoze kutero,” sipamakhalanso mantha. Aloleni iwo abwere, anene chirichonse chimene iwo akufuna. Chikhulupiriro chatu chiri mwa Mulungu, Mulungu yekha. Ife timakhulupirira izo.

46 Panali nthawi imene makhalidwe apa tebulo a fuko lino ankakhazikika pa mawu a mkazi. Ndikukhulupirira kuti dzina lake linali Emily Post. Tsopano, iye anali mtheradi wa makhalidwe apa tebulo. Ngati Emily Post akanati, “Muzitenga ndi kudya nyemba zanu ndi mpeni,” izo zinali chomwecho. Hmm. Izo zinali chomwecho, chifukwa iye anali mtheradi wa makhalidwe apa tebulo. Ngati iye akanati, “Muzimwa khofi wanu kuchokera m’sosala yanu, ndipo muzimwa monga munachitira,” ziribe kanthu kuti zingamveke mwauve bwanji, iyo inali Mtheradibe. Aliyense ankagwadira ku izo chifukwa iwo ankamutenga iye kukhala mtheradi wa makhalidwe apa tebulo.

47 Ife tikuyenera kukhala ndi mtheradi ziribe kanthu zomwe ife tikuchita. Ngati ife titi tidzakwaniritse chirichonse, tikuyenera kukhala ndi mtheradi.

48 Inalipo nthawi imene mawu a Hitler anali mtheradi ku Germany. Zinalibe kanthu chimene wina aliyense ankanena, mawu a Hitler anali mtheradi. Ngati iye anati, “Iwo afe,” iwo ankafa. Ngati iye anati, “Iwo akhale moyo,” iwo ankakhala ndi moyo. Ndipo ngati iye anati, “Ife tipita ku nkondo,” kapena, “Ife sitipita ku nkondo,” chirichonse chimene ife tingachite, mawu ake anali mtheradi.

49 Inalipo nthawi imene Italy inali ndi mtheradi. Amenewo anali mawu a wolamulira mwankhanza wawo, Mussolini, chimene iye anena kuti muchite. Iwo anati womuyendetsa wake anafika, molawirira ndi miniti imodzi, kuti akamutenge iye. Iye anamuwombera iye. Chifukwa chiyani? Iye anati, “Sindikufuna kuti iwe udzifika pano molawirira ndi miniti imodzi. Ine ndikufuna kuti iwe udzifika pano pa dontho, pa nthawiyo ndendende.” Mukuona? Mawu ake anali mtheradi. Italy yense ankagwadira kwa iwo.

50 Inalipo nthawi pamene Farao, mu Igupto, anali mtheradi. Koma inu mukuona . . .

51 Koma ziganizo zonsezi zimene iwo anazipanga zinali ziganizo zopangidwa ndi anthu, ndipo izo zonse zinalephera. Chifukwa chiyani? Chifukwa izo sizinali zogwirizana ndi anthu. . . Izo sizinali zogwirizana ndi Mawu a Mulungu kwa moyo wa munthu. Ine ndikufuna zimenezo, ine ndikuyembekeza, kuti zizikika. Ngati tikuyembekeza kupulumutsa moyo wa munthu, tikuyenera kubwera mogwirizana ndi Mawu a Mulungu ndi dongosolo la Mulungu la moyo wa munthu. Ndipo njira

yokhayo imene inu muti mudzapezere izi, ndi kuzipeza izo mu Mawu Ake, ndi kuzikhulupirira izo.

<sup>52</sup> Tsopano, kotero, Afarao amenewo, ine ndinali ku Igupto osati kale kwambiri, ndipo ine ndikuganiza iwo ankachita kukumba mapazi twente kupita pansu mu nthaka, kuti apeze a—pamalo pamene Farao ankakhala monga mfumu ya dziko lapansi.

<sup>53</sup> Ndi a Herode aakulu, ndi ena otero, kudutsa chotsika kutsatira mzerewo, ife tikuwona pamene maufumu awo anagwera ndi kumapitirira.

<sup>54</sup> Koma pali Ufumu umodzi umene uli pamwamba pa maufumu onse. Iwo ndi wokwera mmwamba kwambiri kukafika mmiyamba mpaka iwo sudzatha konse. Ndipo Uko kukukhala Mfumu, imene, pamene Iyo ipanga lingaliro Lake pa chirichonse, ndipo ife nkukhulupirira lingaliro limenelo, umenewo ndi mtheradi. Izo zidzakhala mwanjira imeneyo mosalabadira chimene wina aliyense anganene za izo. Ndi momwemo nthawizonse.

<sup>55</sup> Tsopano, Khoti lathu Lalikulu. Khoti lathu Lalikulu, ilo—ilo ndi mtheradi, mathero a milandu yonse. Tsopano, ife tiyenera kukhala ndi ilo. Nthawizina ife tikhoza kusagwirizana ndi lingaliro lake. Monga, iwo sanagwirizane ndi la Hitler, ndi ena otero. Komabe ife tikuyenera kukhala ndi mtheradi uyu. Ndipo mtheradi wa fukoli ndi milandu ndi Khothi Lalikulu. Makhothi athu ammada akhoza kuzenga chirichonse ndi kugamula *ichi*, koma Khothi Lalikulu limalamulira pamwamba pa onsewo. Ife tikuyenera kukhala nalo. Monga fuko, ife tikuyenera kukhala ndi lingaliro lake, chifukwa fuko limamangidwa ku mtheradi uwu wa Khothi Lalikulu. Chabwino.

Chirichonse chikuyenera kukhala ndi mtheradi.

<sup>56</sup> Kodi mumadziwa kuti masewera a mpira wamba amayenera kukhala ndi mtheradi? Eya. Kodi mtheradi wa masewero a mpira ndi chiyani? Wa kherere. Bwanji patakhala kuti palibepo wa kherere, mwaona, wa kherere? Ziribe kanthu pamene iwe wayima, ndi malo otani amene iwe ukuyang'anapo ndipo iwe nkudzati, “Iwo unali mpira,” ndipo iye nkuti, “Kunali kumenya,” chabwino, icho ndi chimene chinali, uko kunali kumenya. Chifukwa chiyani? Chifukwa, mawu ake, ziribe kanthu zomwe owonererawo ananena, zomwe winawake ananena, ndi kumenya chifukwa iye anati iko ndi kumenya, ndipo iye ndi wa kherere. Tsopano, bwanji ngati pakanati pasakhale wa kherere? Pakanakhala mkangano woterowo, ndi chirichonse mu phokoso, mpaka inu simungakhale ndi masewero a mpirawo. Chotero, inu mukuyenera kukhala ndi mtheradi, kuti mukhale ndi masewera a mpira. Izo zikuyenera kukhala mwanjira imeneyo.

<sup>57</sup> Tsopano, pakuyenera kukhala mtheradi, mu nyali za pamsewu. Nyali za pamsewu ndi mtheradi, kani, kwa

oyenda pamsewu. Nanga bwanji ngati pakanakhala kuti panalibe nyali za pamsewu? Kapena bwanji ngati nyali za pamsewuzo zikanazima, ndipo inu nkuthamangira mumsewu? Ndipo munthu mmodzi nkumabwera njira *iyi*, ndipo iye nkuti, “Tsopano, ine ndinali pano poyamba. Ine ndikuyenera kudutsa.” Winayo nkudzati, “Ndachedwa ku ntchito.” Kukamba za chisokonezo cha pamsewu, inu mungakhale nacho icho kwenikweni. Koma, mwaona, nyali za pamsewu zimakhazikitsa. Izo ndi mtheradi. Ngati nyali yayaka ya girini, pitani. Ngati yayaka yofiira, imani. Ngati pakanati pasakhalepo chinthu choterocho monga a—nyali za pamsewu, ndiye kuti bwenzi tikukhala ndi chisokonezo cha pamsewu.

<sup>58</sup> Ndipo chimenecho ndicho chiri vuto mu chikhulupiro cha Chikhristu lero. Ife tiri ndi zisokonezo za pamsewu zochuluka, aliyense akudzipangira yekha mtheradi wake.

<sup>59</sup> Pamene, ife tiri ndi Mtheradi mmodzi, ndipo ndiwo Mawu a Mulungu wamoyo. Iwo amakhazikitsa izo kwanthawizonse, ziribe kanthu zomwe wina aliyense anganene.

<sup>60</sup> Izo zafika pafupifupi pa malo monga momwe zinkakhallira mmasiku a Oweruza, aliyense ali naye mtheradi wakewake. Koma izo zonse zimalephera, monga Afarao ndi ena otero.

<sup>61</sup> Koma mtheradi wa Mulungu ndi Mawu Ake. Iye amawapereka Iwo, “Ndipo miyamba ndi dziko lapansi zidzachoka, koma Iwo sadzachoka konse.” Ine ndimazikonda zimenezo.

<sup>62</sup> Tsopano, ife tiribe nthawi yochuluka, kotero ife tingoyang’ana kwa mphindi zochepe kwa anthu ochepe amene anakumana ndi zovuta, ndi za nthawi zimene imfa inali pafupi, monga ife tayimira usikuuno, ndipo iwo anatenga Mtheradi. Tiyeni tikambirane ndi ena a iwo.

<sup>63</sup> Tiyeni tibwerere ku nkhani yakale imene ili yodziwika kwa tonsefe, mmasiku amene tchimo linali litawunjikana mu dziko mpaka Mulungu anadwala ndi kutopa nalo, ndipo dziko linali loti liwonongedwe. Ndipo Mulungu anamupatsa Nowa Mtheradi, amenewo anali Mawu Ake. Ndipo, zinalibe kanthu, mtheradi ameneyo anali wa kupulumutsidwa kwa anthu. Nowa anadziwa kuti dziko lapansi linali loti lifa. Ndipo Mulungu anamupatsa iye mtheradi, ndipo umenewo unali Mawu Ake, tsopano, kuti awapulumentse anthu Ake ku imfa. Tsopano, kodi mtheradiyo anali chiyani, kuti awapulumentse anthu kuchoka ku imfa m’masiku a Nowa? Anali Mawu a Mulungu. Umenewo unali mtheradi, zinalibe kanthu zimene wina aliyense ankanena.

<sup>64</sup> Chimene sayansi inkanena, “Mulibe mvula mmwamba mmenemo. Ife tikhoza kuwombera kumwezi ndi zida zathu. Kulibe mvula kumeneko. Kodi mvulayo igwa bwanji?” Ngati Mulungu ananena kuti kukanadzakhala mvula ikugwa,

Mulungu akanakhoza kuyika mvula mu mlengalenga, ngati Iye ananena chomwecho.

<sup>65</sup> Nowa ankapitiriza ntchito yake, momasuka, ndi kumapanga chingalawa chopulumutsiramo anthu. Pakuti, panali mtheradi utaperekedwa kwa anthu, kuti iwo akanadzapulumsidwa ngati iwo akanatenga njira yoperekedwa ndi Mulungu ya mtheradi ameneyu.

<sup>66</sup> Kotero, pambuyo, pa nthawiyina, pamene ife tavomereza mtheradi. . .Ndikufuna kunena ichi chifukwa cha makolo a ana awa, za chimene ine ndikufuna kuti ndikuwuzeni inu mu kamphindi chabe. Tsopano, ngati a . . .

<sup>67</sup> Nthawizina, pamene ife tavomereza izo, ife timayikidwa pa yesero, kuti awone ngati ife tikuzikhulupirira izo kwenikweni. Ife—ife. . .Mulungu kawirikawiri amachita zimenezo. Ndipo Mulungu amagwira ntchito. . .

<sup>68</sup> Iye sangasinthe dongosolo Lake, chifukwa Mawu Ake ndi Iyemwini. “Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu. Ndipo Mawu anasandulika thupi ndipo anakhala pakati pathu. Yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.” Kotero, nthawizonse ndi Mulungu.

<sup>69</sup> Pamene Iye ayitanidwa pa chochitika, kuti achitepo, ndipo lingaliro limene Iye amapanga, Iye amayenera kukhalabe ndi lingaliro limenelo. Iye sangathe kulisintha ilo, chifukwa Iye ndi wopandamalire.

<sup>70</sup> Tsopano, ine ndikhoza kusintha lingaliro langa, inu mukhoza, chifukwa ife tiri ndi malire. Chotero, ife timalakwitsa.

<sup>71</sup> Koma Mulungu sangasinthe lingaliro Lake, chifukwa Iye ndi wopandamalire, ndipo Lake—lingaliro Lake limakhala langwiro, nthawizonse. Iye sangakhoze kunena kuti, “Ine ndinalakwitsa *apa*, ndipo Ine ndisintha lingaliro Langa,” chifukwa izo zingasonyezere kuti Mulungu akhoza kusintha. Ndipo Mulungu sangasinthe, ngakhalenso Mawu Ake sangasinthe. Iye ali yemweyo, nthawizonse.

<sup>72</sup> Chotero, Mulungu anampatsa Nowa yesero, atatha kuvomereza mtheradi Wake. Nowa analowa mu chingalawa. Mulungu anatseka chitseko kumbuyo kwake. Mosakayikira iwo anati, “Tsopano, m’mawa, kudzakhala mitambo yakuda. Ndipo kudzakhala mabingu ndi mphezi, ndipo mvula idzagwa.” Koma, inu mukudziwa, tsiku lotsatira, dzuwa linatuluka mowala basi monga ilo linayamba lachitirapo.

<sup>73</sup> Ine ndikulingalira, okhulupirira ammalire anati, “Ife tipita kumeneko. Bambo wokalambayo akhoza kukhala kuti amalondola za izo. Kotero, mwinamwake sayansi imalakwitsa, kuti uko—kukhoza kukhala mvula ina kumwamba kumeneko.” Koma, kumbukirani, iyo inali isanavumbepo.

<sup>74</sup> Koma, kenako, tsiku lachiwiri, dzuwa linali lowala basi monga ilo limakhalira nthawizonse; lachitatu, lachinayi, lachisanu, lachisanu ndi chimodzi, ndipo mpaka tsiku lachisanu ndi chiwiri. Koma Nowa anali atakwera mchipinda chapamwamba, kuti azitha kuyang'ana mumlengalenga. Ndipo mmawa wa lachisanu ndi chiwiri lija, pamene inadzafika nthawi, pamene anthu anali atakana njira ya mtheradi ya Mulungu ya chipulumutso, yopulumutsira miyoyo ya anthu, mvula inayamba kuvumba ndipo ngalande zinadzadza. Ndipo a—ngalawayo inayamba kunyamuka, ndipo inamutengera Nowa ndi iwo ku chitetezero. Ndithudi, chifukwa iwo ankadalira mu Mawu a Mulungu, mtheradi, Mawu a lonjezo a Mulungu.

<sup>75</sup> Ziribe kanthu momwe izo zikuwonekera moyipa, ndi momwe kuliri mdima, khulupiriranibe mtheradi wanu.

<sup>76</sup> Mose, bwanji, wake, iye anali atayesetsa kuti apulumutse moyo wa Ahebri osauka amenewo. Ndipo iwo anali pafupifupi moyipa, kapena moyipa basi, monga momwe ana awiri awa aliri amene ife tikuyesetsa kuti tiwapulumutse usikuuno. Iwo anali akapolo, ndipo iwo ankawapha iwo mwachisawawa basi, nthawi iliyonse imene iwo ankafuna kutero. Ndipo Mose anamverera mu mtima mwake kuti icho sichinali—chifuniro cha Mulungu. Chotero, iye—iye anayesetsa kuchita izo kupyolera mu maphunziro. Iye anayesetsa kuchita zimenezo mwa kuyesetsa kwake komwe, ndipo iye anapeza kuti analephera momvetsa chisoni. Iye anachita chinachake iyemwini chimene sichinali cholondola, chifukwa iye anamupha munthu wina. Ndipo chimenecho sichinali cholondola.

<sup>77</sup> Kenako, iye anapita mchipululu ndipo anakakhala kumeneko kwa zaka forte. Koma, tsiku lina, iye ankaweta nkhusa kuseri kwa chipululu, ndipo panali Kuwala mu chitsamba. Ndipo pamene Mose anafika pafupi ndi Kuwala uku, Liwu la Mulungu linayankhula kwa iye kuchokera mu Lawi la Moto ili liri kumbuyo mu chitsamba ichi, ndipo linati, “Mose. Mose.”

Ndipo iye anati, “Ndi ine pano, Ambuye.”

<sup>78</sup> Ndipo Iye anati, “Vula nsapato zako, pakuti malo amene wayimapo ndi opatulika. Ine ndamva kubuula kwa anthu Anga. Ine ndamva msonkhano wawo wa mapemphero. Ndakumbukira kuti ndinawalonjeza iwo.” Mai, ngati izo sizingayike mitima ya okhulupirira Achikhristu pamoto usikuuno! “Ine ndi Mulungu. Ndakumbukira kuti ndinalonjeza izo.” Momwe Liwu limenelo linaliri la Malemba! Ndipo Iye anati, “Mose, Ine ndikukutuma iwe kumusi uko kuti ukawapulumutse iwo.” Ndipo Mose . . .

<sup>79</sup> Chifukwa, monga ine ndinanenera pachiyambi, pamene iwe utenga mtheradi ameneyo wa Mulungu, iye amakupangitsa iwe kuchita zinthu zimene, chabwino, nthawizina zoseketsa, pamaso pa anthu. Kodi inu mungalingalire, munthu amene anali

atathawa kwa Aigupto, mmawa wotsatira, atatha kuwuwona mtheradi uwu. . .

<sup>80</sup> Mawu a Mulungu awa anayankhula kwa iye umboni wotsimikizika, chifukwa anali Mawu. Lonjezo linali pamene, ndi kutsimikizira kwa Mulungu wamkulu wa chirengedwe, momwe iye anachitira chozizwitsa pa—pamaso pa Mose, ndipo anawonetsera kuti Iye anali Mulungu wachirengedwe.

<sup>81</sup> Ndipo Mose, mmawa wotsatira, anamutenga mkazi wake ndipo anamukweza iye pa bulu, ndi—mwanayo m'chiuno mwake. Ndipo wa zaka-eyite-zakubadwa, ndevu zikulendewera mpaka m'chiuno mwake, mutu wake wadanzi ukunyezimira, ali ndi ndodo yokhota m'dzanja lake, akupita kumusi chaku Igupto, akufuula mwamphamvu momwe iye akanathera.

“Iwe ukupita kuti, Mose?”

“Ine ndikupita uko ku Igupto, kukalanda.”

“Kukalanda?”

<sup>82</sup> Kuwukira kwa munthu mmodzi! Chifukwa chiyani? Iye anali ndi mtheradi. Iye anali ndi chinachake. Iye anali ndi Mawu a Mulungu, iye akanakhoza kuyimapo. Mwamuna wa zaka eyite zakubadwa, ali ndi bulu, ndi ndodo m'dzanja lake. Ndizo zonse zimene iye anali nazo. Monga kuwukira kwa munthu m'modzi ku Russia, lero. Koma iye anapita kumeneko ndipo anakalanda, chifukwa iye anali ndi mtheradi. Iye anali atayankhulana ndi Mulungu. Iye anali atamva Liwu la Mulungu. Ndipo iye. . . Chinthu chake chinali chakuti, iye anachita zimenezo. Kulondola. Chifukwa chiyani? Icho chinali ndi iye masiku onse a moyo wake. Uyo anali mtheradi.

<sup>83</sup> Palibe munthu amene ali ndi ufulu wokwera pa guwa, kukalalikira Uthenga, pokhapokha iyemwini atayendapo pa mchanga wopatulikawo, pamene palibe wotsutsa kapena wosakhulupirira angakhoze kufotokoza konse motsutsa chazimu cha Mulungu. Yesu sakanawalola ophunzira Ake kuti azilalikira, zinalibe kanthu momwe iwo ankamudziwira Iye bwino; iwo ankayenera kupita ku mzinda wa Yerusalemu, kumeneko kukadikirira mpaka iwo atadzazidwa ndi Mphamvu yochokera Kumwamba. Iwo ankayenera kukhala ndi chowachitikira chimenecho.

<sup>84</sup> Mose, podziwa kuti iye anali mneneri, ankadziwa kuti iye analeredwa kwa cholinga ichi, koma popanda kukhudza kwake kwake kumeneko, Mtheradi umenewo, chinachake chimene chinatsimikizira kwa iye kuti pamene iye anapita kumeneko, iye akanakakhala ndi chiwombolo cha anthu awa. Iye sanali konse chimodzimodzi. Iye anapita kumeneko chifukwa iye anali ndi mtheradi, ndipo iye anakachita chimodzimodzi basi chimene Mulungu anamuwuzwa iye kuti akachite. Munalibe mantha mu mtima mwake, pamene iye anaponyera pansu njokazo, kapena ndodozo, ndipo izo zinasanduka njoka. Ndipo otsanzira

achithupithupi anabwera ndi mtundu wawo wa utumiki, ndipo anaponyera pansu ndi kuchita chinthu chomwecho. Mose anali atachita ndendende basi chimene Mulungu anamuwuzwa iye kuti achite. Panalibe chirichonse kwa iye choti achite koma kuyima chiriri ndi kuwona ulemelero wa Mulungu. Ndiye ife tikupeza kuti Mulungu anatenga njoka yake ndipo inadya zina zonsezo. Umo ndi momwe izo zimachitikira. Iye anali wotsimikiza kuti Mulungu amene anamuwuzwa kuti achite izi, akanatha kumusamalira iye mu nyengo yovuta.

<sup>85</sup> Kodi ife sitingathe usikuuno, pa maziko a mnyamata ameneyo akupereka mtima wake kwa Khristu, tiyime pa mtheradi uwu, kuti Mulungu akhoza kupanga zosatheka kukhala zotheka! Iye akhoza kusintha mitima ya oweruza! Nchifukwa chiyani ife timadumphwa mwamantha, za zinthu zina? Tiyeni timutenge Mulungu, poyamba. Tizibweretsenso izo ku lonjezo. Mulungu analonjeza izo, kuti—kuti Iye akanadzachita izo.

<sup>86</sup> Chotero, kumbukirani, Mose nthawizonse anali munthu wosinthika chifukwa iye ankatenga Mawu a Mulungu ndi kuwakhulupirira Iwo. Ndipo iye anali ndi lonjezo lotsimikiziridwa kwa iye.

Ndi angati amene ife tikanakhoza kuwatchula? Ife tiribe nthawi.

<sup>87</sup> Polemba pa kapepala, lero, ndimalemba apa za Daniele, momwe izo zinali, chimene izo zinali, icho chinali chilango cha imfa kwa iye kuti—kuti apemphere kwa mulungu wina aliyense. Koma iye anali atalumikizana ndi Mulungu, ndipo iye ankadziwa kuti Mulungu anali wokhoza kumusamalira iye.

<sup>88</sup> Ana Achihebri, iwo akanadzaponyedwa mu ng'anjo yamoto ndipo akanawotchedwa ndi kutentha, kutentha kaseveni kuposa momwe ng'anjonyo inatentherapo. Ana Achihebri aja anamukhulupirira Mulungu. Iwo anati, “Mulungu wathu ndi wokhoza kutipulumutsa ife ku ng'anjo iyi.” Chifukwa chiyani? Iwo anali ndi mtheradi. Iwo anali ndi Mawu a Mulungu.

<sup>89</sup> Ndipo Mulungu amene akanakhoza kuwawombola ana Achihebri amenewo ku ndende ya imfa ya ng'anjo yamoto, ndi mochuluka bwanji momwe Iye angakhazere kuwombola mnyamata wamng'ono Wachiyuda uyu kunjira kuno, amene ali uko mu ndende ya imfa? Ndi mochuluka bwanji Iye. . . Ndipo Iye akadali Yehova Mulungu yemweyo amene Iye anali nthawizonse. Ife, monga mtumwi Paulo, tikhoza kuzindikira kuti Mulungu yemweyo ali moyo lero, “Dzulo, lero, ndi kwanthawizonse yemweyo.” Ndiyeno, Akhristu akhoza kugwira dzanja losasintha la Mulungu, ndi kusintha chochitika chonsecho. Pemphero limasintha zinthu. Icho ndi chimene ife tikufuna kuchita.

<sup>90</sup> Kodi tinganene bwanji za Yoswa? Iye awoloka bwanji Yordano? Zikuwoneka ngati Mulungu anali msirikali

wachilendo, mu mwezi wa Epulo momwe, pamene madzi anali atasefukira monga chomwecho. Koma Iye anati kwa Yoswa, “Tenga likasalo ndipo upite patsogolo.” Ndizo zonse zomwe iye ankayenera kuti achite. Ndipo Mulungu anasunthira Yordano mmbuyo ndipo anapanga malo owuma, ndipo iwo anawoloka ndipo anapulumutsidwa. Izo zinachitika motani!

<sup>91</sup> Nzosadabwitsa Yoswa anati, “Ine ndi nyumba yanga, tidzamutumikira Ambuye.”

<sup>92</sup> Momwe Davide, mbadwa yaikulu ija, momwe ife tikanafunira kuyankhula za iye, ife tiribe nthawi, koma, ndipo nthawi zambiri, monga tinamumva winawake akuyankhula mphindi zingapo zapitazo zokhudza Davide ndi tchimo lake, koma pamene, zonse za izo zinakhululukidwa, pamene iye ankapita ku nkondo, ndipo ife timazitcha izo mu dziko, “zinthu zinafika povuta,” ndipo kutsutsa kunali kwakukulu, ndipo Davide anagona pamenepo pansi pa mtengo, ndipo anatuluka thukuta, mpaka iye anamva phokoso likudutsa mu tchire la mabulosi, ndiye izo zinali zosiyanana. Davide anadzuka ndipo anapitirira, chifukwa chakuti iye anali ndi mtheradi, mwakuti iye ankadziwa kuti uyo anali Mulungu akupita patsogolo pake.

<sup>93</sup> Kodi ife sitingapemphere pemphero la chikhulupiro limene liti limutumize Mulungu kwa oweruza kumusi uko? Ndithudi, ife tikhoza. Ife tikukhulupirira kuti ife tikhoza, ngati ife titi tigwiritsitse ku mtheradi ameneyo.

<sup>94</sup> “Momwe Abrahamu anazitchulira zinthu, zomwe kunalibe, ngati kuti zinalipo,” chifukwa iye anali ndi lonjezo la mtheradi lochokera kwa Mulungu, kuti Mulungu akanati amupatse iye wake. . . kumupatsa iye mwana kupyolera mwa Sarah. Ndipo pamene mkaziyo anali usinkhu wa zaka handirede, kapena iye anali, ndipo mkaziyo anali nainte, “Iye sanagwedezekebe pa lonjezo la Mulungu mwa kusakhulupirira, koma anali wamphamvu, akupereka matamando kwa Mulungu.” Ndipo ife timadzinenera kuti ndife ana a Abrahamu. Pamene Abrahamu. . .

<sup>95</sup> Pamene, ife takhalapo nalo Baibulo lolembedwa kuyambira mmasiku a Abrahamu, ndi mboni zonse zimene ife takhala nazo kumbuyoku, kuti Yehova amasunga Mawu Ake, kuti Khristu ndi Mwana wa Mulungu. Iye ndi Mkhalapakati pakati pa munthu ndi Mulungu, ndipo palibe mkhalapakati wina kupatula Iye. Ndi kulonjeza, “Ngati inu muwapempha Atate chirichonse mu Dzina Langa, icho chidzaperekedwa.” Ndipo ife timadzinenera kuti ndife ana a Abrahamu. Pamene, “Abrahamu anazitcha zinthu, zimene zinalipo, ngati kuti panalibe, chifukwa iye anakhulupirira Mulungu.” Mwamtheradi. Ine ndikukhulupirira izo ndi mtima wanga wonse.

Moyo wa Paulo wokhazikika pa Khristu unali mtheradi wake. Iwo unamumangirira iye.

<sup>96</sup> Khristu anali mtheradi wa chiwukitsiro, monga tikuwerengera apa. Iye anati, “Mulungu analumbira mwa lumbiro, kwa Davide, kuti sadzasiya solo yake mu gehena.” Lumbiro ndi mapeto a mikangano yonse. “Ndipo Iye analumbira kuti Iye sadzasiya solo Yake mu gehena, koma kuti adzamuwukitsa Iye.” Ndipo chotero Iye anamudalira Mulungu, ndipo anapachikidwa; anafa, anawukanso, ndipo anakwera Kumwamba, chifukwa Iye anakhulupirira Mulungu.

<sup>97</sup> Ndi mochuluka bwanji, pamene Iye akupereka chitsanzo, momwe ife tingatengere mtheradi! Ngati Khristu anamutenga iye, pa lonjezo limodzi limenelo pamenepo, ndi mochuluka bwanji momwe ife tingathe kumutenga iye, ndi masauzande a malonjezo! Ndipo ndi Magazi a Yesu Khristu pamenepo kuti ayeretse njira yathu, ndi kutiwolotsa ife pa phompho lalikulu lija la tchimo limene linatilekanitsa ife, la kusakhulupirira, kuchokera kwa Mulungu, ndi kutibweretsa ife mu Kukhalapo Kwake komwe, kuti tiyankhulane ndi Iye, izo zikanakhala mochuluka bwanji! Inde. Ife tikuyenera kukhala nawo mtheradi.

<sup>98</sup> Ine ndikuganiza za mmodzi pakali pano, monga potseka, angakhale George Washington, pamene Amerika anali wamng’ono ndipo ife tinkamenyera moyo, moyo wa fuko lalikulu ili limene ife tiri nalo. George Washington anali Mkhristu. Iye anali wokhulupirira. Ndipo kumusi ku Valley Forge, ine ndimawuzidwa kuti asilikali Achimerika anali kokha, pafupifupi gawo limodzi mwa magawo atatu a iwo, anali atavala nsapato. Ndipo nyengo yachisanu inali yozizira, ndi nyengo ya ziro, ndipo mtsinje utawuma ndi kusefukira. Ndi achi British kumbali inayo. Ndipo moyo wa fuko laling’ono ili unali pafupi.

<sup>99</sup> Kodi iye anachita chiyani? Iye anali Mkhristu. Iye anapita kunja usiku ndi kukagwada pansu mu chisanu, ndipo anapemphera mpaka kunyowa ndi madzi a chisanu atakwera kuzungulira mchiuno chake. Ndipo iye anakhala pamenepo ndipo anapemphera mpaka iye anapeza mtheradi, yankho lochokera kwa Mulungu, kuti Mulungu akanati amupatse iye chigonjetso.

<sup>100</sup> Ndipo tsiku lotsatira, Valley Forge sanali kanthu kwa iye. Iye anawoloka Delaware, anakankha kudutsa mu chisanu ndi asilikali ovala mwatheka, atawuma mwatheka, mapazi awo opanda nsapato ali pansu, mu chisanu. Ndipo iye anatenga iyo, pamene zipolopolo zitatu zamfuti zinadutsa mu chikhotho chake. Chifukwa chiyani? Iye ankadalira mu mtheradi wa pemphero loyankhidwa. Amen. Maziko omwe a fuko lathu anakhazikika pa chinthu choterocho.

<sup>101</sup> Kodi vuto ndi chiyani ndi anthu lero amene amadzinenera kuti ndi Akhristu? Nchifukwa chiyani tasokonezeka mu ora

ngati ili? Tiyeni tisasokonezeke. Tiyeni tikhale asilikali. Inde, bwana.

<sup>102</sup> Iye anapemphera mpaka anapeza yankho limenelo. Ndiye, panalibe mtsinje wantambo, panalibe asilikali opanda nsapato, mosalabadira za nyengozo, iwo akanakhoza kutenga iwo chifukwa Mulungu anali atanena chomwecho. Chipolopolo sichikanatha ngakhale kumupha iye, kuchokera ku mfuti ya mdani. Ndithudi. Chifukwa chiyani? Iye anali ndi msonkhano wapemphero. Iye anapeza yankho.

<sup>103</sup> Momwe izo zinaliri zabwino usiku wina, pamene mtumwi Petro anali mu ndende, ndipo iwo anali oti amuphe iye m'mawa mwake. Iye anali woti afa pansi pa chilango cha imfa, monga Myuda wamng'ono uyu ali woti achitidwe tsopano. Koma kodi iwo anachita chiyani? Iwo anachita chinthu chomwecho chimene ife kuno ku Houston tikuyesera kuti tichite. Iwo anapanga msonkhano wa mapemphero ku nyumba ya Yohane Marko. Pamene iwo anali kupemphera, Mngelo wa Ambuye anapita ku ndende, ndipo anakatsegula zitsulo za ndende, ndipo anatsogola zipata. Ndipo kupitirira izo, anamutsogolera Petro kunja, ndipo anabwera mpaka ku msonkhano wa pemphero komwe.

<sup>104</sup> Ine ndikukhulupirira, usikuuno, kuti Mulungu yemweyo ali moyo. Ngati Iye siali Mulungu yemweyo, ndiye kuti pali chinachake cholakwika. Ndithudi.

<sup>105</sup> Kodi izo zinachitidwa bwanji? Mwa msonkhano wa mapemphero, mwa Akhristu okhulupirika amene ankakhulupirira, ndipo anakhulupirira kuti Mulungu akanamuwombola m'bale wawo ku chilango cha imfa. Iwowo anali Akhristu amene anakhala usiku wonse ndipo anagona pa nkhope zawo, ndipo anafuula ndi kupemphera.

<sup>106</sup> Monga ine ndinamumvera mmodzi wa atumiki, kanthawi kapitako, akunena kuti iye akanati afuule, utali wa usiku wonse. Vuto lake ndi lakuti, lero, anthu amalekerera. Iwo amatopa, amagona. Iwo sangathe ngakhale kukhala mu msonkhano wa maminiti teni, nkomwe. Chabwino, icho—icho ndi chinachake cholakwika.

<sup>107</sup> Ngati mumamukonda Mulungu, chabwino, ife tikuyenera kukhala otanganidwa. Zikuyenera kukhala zathu—ziyembekezo zathu, zokhumba zathu. Izo zikuyenera kukhala. Chirichonse chimene chiri mwa ife chikuyenera kukhala mu chikondi cha Khristu. Ameni. Ife timakhala mwaulesi kwambiri. Ife timakhala osakhudzidwa kwambiri, pamene dziko likufa pansi pa mapazi athu. Uko nkulondola. Miyoyo ya anthu ikutuluka, opanda Mulungu, ndipo ife timakhala chomwecho—zosatikhudza kwambiri za zimenezo. Bola ngati ife tiri a mpingo, ndizo zonse zimene timaganiza kuti zimapangitsa kusiyantsa.

<sup>108</sup> Ine ndimayankhula za Kudza kwa Khristu, masabata angapo apitawo, mu mpingo winawake. Ndipo zitatha izo panali

wina amene anakomana nane kuseri kwa tchalitchi, ndipo anati, “M’bale Branham, inu mumawawopsyeza anthu mpaka pafupi kufa.”

Ine ndinati, “Nchifukwa chiyani ine ndimachita zimenezo?”

<sup>109</sup> Iye anati, “Chabwino, inu mukuyankhula za Kudza kwa Khristu. Ine sindikufuna kumamva zinthu zoterozo monga izo. Ine ndiri ndi mnyamata wamng’ono pano amene ine ndikuyenera kumulera. Ine ndiri ndi mtsikana ku sukulu.”

<sup>110</sup> “Oh,” ine ndinati, “Kudza kwa Khristu ndi chinthu chaulemerero kwambiri chimene ine ndingachiganizire.” Ndithudi. Mukuona?

<sup>111</sup> Baibulo linati, “Onse amene *amakonda* kuwonekera Kwake.” Oh, mai, tsiku limene chivundi chakale ichi chidzatenga chisavundi, ndi iyi—nyumba ya tizilombo iyi imene ndikukhalamo idzasinthidwa, mu kamphindi, mu kuthwanima kwa diso, ndi thupi ngati thupi Lake Lomwe laulemelo! Icho chikuyenera kukhala chokhumba cha mtima wa Mpingo. Mwamuna ndi mkazi aliyense akuyenera, kukhala pamoto, akulalikira m’misewu ndi kwina kulikonseko, akuyesetsa kuti apulumutse miyoyo. Ndithudi.

<sup>112</sup> Ine ndikudabwa ngati ife tamangirizidwa kwenikweni ku mtheradi umenewo umene ife timadzinenera kuti tatero. Kodi ife tikuyang’ana pa nyenyezi yoyenera yaku m’mawa? Ngati ife tikungodalira mu mpingo wathu ndi chipembedzo chathu, mgwirizano wathu; pamene dziko likusinthwa, izo zimasinthwa ndi ilo, kuzungulira ndi kuzungulira.

<sup>113</sup> Koma pali Nyenyezi imodzi imene simasintha nkomwe. Pali chinthu chimodzi chimene sichingasithe, ameneyo ndi Mulungu. Mulungu sangasithe. Mawu Ake sangasithe. Baibulo Lake silingasithe. Ndipo ngati munthu wabadwa mwa Mzimu wa Mulungu, ndi Khristu mwa iye, amavomereza lonjezo lililonse ndi “ameni.” Izo nzoona. Ndithudi.

<sup>114</sup> Oh, ndithudi, msonkhano wa pemphero ndi chimene ife tikuchisowa. Ife tikuyenera kukhala Akhristu. Akhristu onse akuyenera kugwiritsa ntchito Mtheradi womwewu, Mawu a Mulungu. Mawu a Mulungu ndi pamene amakhalapo Mkristu.

<sup>115</sup> Yesu anati, m’Mawu Ake, “Ngati inu mukhala mwa Ine, Mawu Anga nkukhala mwa inu, ndiye inu mukhoza kupempha chimene mukuchifuna, ndipo chidzachitidwa kwa inu.” Taganizani za izo. Inu mungafune bwanji mtheradi winanso? Kodi inu mungadalire chiyani chinanso kuposa chinachake monga chimenecho? “Ngati inu mukhala mwa Ine, Mawu Anga nkukhala mwa inu, ndiye pemphani chimene mukufuna.”

<sup>116</sup> Kumupempha Mulungu kuti agwire ntchito pa mtima wa woweruza ameneyo, kapena gulu la okhululukira milandu

lija, ndi kumuchotsa mnyamata wamng'ono uyo mu chipinda cha okaphedwa chimenecho, ngati ife tingapemphe izo ndi chikhulupiriro, tikukhulupirira, mu misonkhano ya pemphero iyi, ife tipeza izo. Ndizo, ine ndimangomukhulupirira Mulungu monga chomwecho.

<sup>117</sup> Ndipo chikhulupiriro changa chimene ine ndiri nacho mwa Mulungu, icho ndi chifukwa chimene ine ndiri pano usikuuno. Ndi chifukwa chake ndinaimitsa chinachake, ndi kudzafika kuno. Ine ndikuyenera kuyendetsa mahandirede a mamailosi usikuuno, kubwerera ku Tucson, Arizona, chifukwa ine ndabwera kuti ndidzayike chikhulupiriro changa ndi chanu. Ameneyo ndi munthu. Ndi solo ili kumeneko. Ndi winawake amene akusowa. Ndipo ife Akhristu tikuyenera kudzuka ku zenizeni, ku chenicheni, chikhulupiriro chenicheni, kuchimangirira icho ku Mawu a Mulungu, ndi kuchonderera lonjezo limenelo. Inde, bwana. Oh, mai! “Ngati inu mukhala mwa Ine, ndi Mawu Anga mwa inu, pemphani chimene mukuchifuna.”

<sup>118</sup> Ndipo kachiwiri, “Ngati anthu amene amatchedwa ndi Dzina Langa adzasonkhana pamodzi ndi kupemphera, ndiye Ine ndidzamva kuchokera Kumwamba.” Msonkhano wa pemphero, ndi zimenezotu.

<sup>119</sup> Ine ndimakhulupirira mu kuyankhulana ndi oyimira milandu ndi kuyankhulana ndi maloya, kapena oweruza, kapena mabungwe okhulukira milandu, kapena china chirichonse. Izo zonse nzabwino. Koma, m'bale, ngati chiyembekezo chanu sichinamangidwe ku chinachake choposa anthu amalingaliro achithupithupi chabe, kapena, malingaliro a anthu, kani, inu ndithudi mudzakhumudwitsidwa momvetsa chisoni.

<sup>120</sup> Koma ngati inu mungamangirire chikhulupiriro chanu pa malo otero amene inu mukuwadziwa, ndi kukhala pamenepo ndi kupemphera mpaka Mulungu atayankha, ndipo inu nkudziwa kuti muli nacho mu mtima mwanu, chinachake chichitika.

<sup>121</sup> Ine ndawonapo akufa akuwukitsidwa kuchokera ku nyumba yamaliro. Ine ndawonapo—maso akhungu akutseguka, makutu ogontha akumva. Ine ndawonapo matenda odzaza ndi khansa, ndi khansa ya sarcoma, khate, akuchiritsidwa ndi mphamvu ya Mulungu Wamphamvuzonse. Chifukwa, iwo anali ndi chikhulupiriro chokhulupirira kuti Mulungu ameneyo, Amene anapanga lonjezo, akanatha kudzasunga lonjezo Lake. Chimenecho ndi chenicheni, chikhulupiriro chenicheni chonga Abrahamu anali nacho.

<sup>122</sup> Kumangirira pamenepo. Kukhala pamenepo ndi kupemphera. Osati kungogwada pansu, nkuti, “Mulungu, mpulumutseni munthu wamng'ono wosaukayo ndipo mtumizeni iye kwawo.” Ife tonse tingazikonde zimenezo. Koma tiyeni tikhale pamenepo mpaka chinachake chitachitika. Oh! Pamene

chinachake chichitika, ndiye, chitsimikizo chimenecho chikhoza kugwera pakati pa anthu apang'ono awa amene akhala mu holo muno usikuuno, chikhoza kugwera pakati pathu pomwe pano, chikhulupiriro chokwanira ndi mphamvu ya Mulungu, ngati ife tingakhoze kupemphera mobowoleza, mpaka ife titakhudza mzere wa kwathu uwo, mpaka mtheradi ameneyo atatsika pansi, Lawi la Moto lomwelo limene linatengedwa kuno mu Houston, ndi kamera ya Ted Kipperman, zaka thwelovu zapitazo. Iye ali pano usikuuno, wamkulu basi monga Iye anali nthawi imeneyo, kuti amuwombole mnyamata ameneyo, ngati ife titangokhulupirira izo, chifukwa Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ine ndikukhulupirira izo ndi mtima wanga wonse. Ichu ndi chifukwa chimene ine ndiri pano kudzapereka pemphero langa ndi inu nonse kuti Mulungu apulumutse moyo wawo.

<sup>123</sup> Ndiye ngati inu mungakhoze kupemphera mobowoleza, mpaka inu mutalandira yankholo, kupezanso chitsimikizochu, monga Washington anali nacho, monga Yohane Marko anali nacho, monga Daniele anali nacho, monga Mose anali nacho, mpaka inu mutapeza mtheradi, chinachake chimene inu mukudziwa kuti mukhoza kumangirirako, ndiye, "Pa Mtheradi uyu Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga," ndipo mabwalo amilandu onse mdziko sangakane Ichu. Uko nkulondola. Pa Ichu!

<sup>124</sup> Mulungu yemweyo amene anakhoza kumutenga Myuda wamng'ono wamphuno yangowe ameneyo ngati Paulo, atakwiya ndipo akupita kumusi kumeneko kukapha Akhristu onse pansi pa chilango cha imfa, ndipo anakhoza kumusinthia iye ndi kumupanga iye kukhala Mkhristu wokondeka, Mulungu yemweyo ali moyo usikuuno, akhoza kusinthia lamulo kukhala chisomo, nthawi iliyonse imene Iye atenga lingaliro kuti achite zimenezo. Aleluya! Munditcha ine woyera-wodzigudubuzwa, mulimonse, kotero ine ndikhoza kungoyamba mu izo pakali pano. Ine ndimamukhulupirira Mulungu ameneyo. Amen. Inde, bwana.

<sup>125</sup> Ndiyeno Marko 11:22, pamene inu munapemphera mobowoleza. Iye anati, "Indetu, indetu, ndinena kwa inu, khalani ndi chikhulupiriro mwa Mulungu. Ine ndinena ndi inu, ngati mudzanena kwa phiri ili, 'Sunthidwa.'" Pamene mtheradi ameneyo wabwera kwa inu, pamene inu mwadzozedwa ndi Mzimu umenewo izo zimabwera kupyola ulamuliro wonse wa sayansi uko, kusanakhale atomu kapena molekyulu, Ameneyo amene anayankhula chirichonse kuti chikhalepo, ndipo pamene solo yanu yazikika kwa ameneyo, palibe chirichonse chimene chingaletse ichu. Uko nkulondola. "Nenani kwa phiri ili, 'Suntha,' ndipo osakaikira mu mtima mwanu, koma kukhulupirira kuti chimene mwanenacho chidzachitika, mukhoza kulandira chimene inu mwanena." Ngati uyo si


mtheradi woti tigwireko! Ndithudi, uyo ali. Uko nkulondola, mtheradi.

<sup>126</sup> Tsopano, fuko liri naye mtheradi. Moyo wakunyumba kwanu uli naye mtheradi. Kulikonse, ngati icho chiri choti chidzakwaniritse chirichonse, icho chikuyenera kukhala ndi mtheradi.

<sup>127</sup> Ife tikumuyamikira woyimira milandu uyu. Ife tikuyamikira, oh, amuna ena onsewo. Wopempheretsa wabwino uyu kuno wochokera ku California, ndipo uthenga wopambana bwanji! Ndi—ndi m'bale wathu amene anayetsa kutenga ndalama ndi chirichonse, kuyetsa kuti amuthandizire mkazi wosawuka uyu, ndi—ndi ana ake, kuti awapulmutse iwo. Zonsezo ndi zabwino. Ife tikuyamikira zimenezo, ndipo ndine wa zimenezo.

<sup>128</sup> Koma pali chinthu chimodzi chopitirira zimenezo, amzanga, pamene ife tikutseka msonkhano uno usikuuno: Ife tikuyenera kumangiriza izo ku mtheradi, msonkhano wa pemphero pamaso pa Mulungu, umene uti utumize chiwombolo kuchokera kwa Yehova Mulungu yemweyo. Iye ali Mulungu mochuluka usikuuno monga Iye anali nthawi imeneyo. Aleluya! Kodi inu mukukhulupirira zimenezo?

<sup>129</sup> Tiyeni tiyimirire pa mapazi athu, ndiye, ndipo usikuuno tipange msonkhano wa pemphero muno, mpakana mtheradi achitike. Kwezani mmwamba manja athu pamaso pa Mulungu. Mupemphere mpaka mutakhudza pachimake, mpaka mtheradi agwere mu mtima mwanu.

<sup>130</sup> Ambuye Mulungu, mutumize Mzimu Woyera Wanu pansu, ndipo mutumize ndi kuwamasula ana awo uko, Ambuye. Iwo akukhala mu zigawo za mithunzi ya imfa. Chinachake chikukonzekera kuti chichitike, Ambuye, ndipo ife tikupemphera kuti misonkhano ya pemphero iyi ikhudze Moto. Ine ndikukukhulupirirani Inu, Ambuye. Ine ndikuzilandira zimenezo, ndipo ine ndikukhulupirira kuti Inu muwawombola ana amenewo. Perekani izi, Mulungu Wamphamvuzonse. Ife, Mpingo Wanu, tikupempha izi, kupyolera mwa Yesu Khristu. Amenii. 

63-0304 Mtheradi  
City Auditorium  
Houston, Texas U.S.A.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

[www.branham.org](http://www.branham.org)